Ambuye wathu Yesu Khristu akubwelaso pa dziko lino la pansi posachedwapa. Ili ndi longezo lomwe adapeleka adakali pa dziko pano zaka zikwi ziwiri (2000) zapitazo (Yoh 14:1-3). Nanga tingatsimikize bwanji kuti iye akudzadi? Chonde welengani zomwe adalosela okha Ambuye Yesu khristu za zomwe zizachitike m'masiku omaliza. Kuwelenga malembowa mosamala ndikufananiza ndi zomwe zikuchitika mu dzikoli lelo, zititsimikizila kuti Ambuye Yesu Khristu adzadi mu nthawi yomwe tilikukhalayi.

## 1 CHIONONGEKO CHA KACHISI

Ndipo pamene analikutuluka Iye m'Kachisi, m'modzi wa ophunzira ache ananena kwa Iye, Mphunzitsi, onani, miyala yotere ndi nyumba yotere. Ndipo Yesu anati kwa iye, Kodi waona nyumba izi zazikuru? Sudzasiyidwa pano mwala umodzi pamwamba pa unzache, umene sudzagwetsedwa. (Mat 24:1-2; Marko 13:1-2; Luka 21:5-6). **Izi zidakwaniritsidwadi mu chaka cha 70 A.D.**

## 2 ZIZINDIKILO ZA KUBWELA KWAKE

Ndipo pamene anakhala Iye pa phiri la Azitona, popenyana ndi kachisi, anamfunsa Iye pa yekha Petro, ndi Yakobo, ndi Yohane, ndi Andreya, kuti, Tiuzeni zinthu izi zidzachitika liti? Ndi chotani chizindikilo chache chakuti ziri pafupi pa kumalizidwa zinthu izi zonse? (Mat 24:3; Marko 13:3-4; Luka 21:7)

## 3 OSOCHERETSA AZAUKA

Ndipo Yesu anayamba kunena nawo, yang'anirani kuti munthu asakusochereseni. Ambiri adzafika m'dzina langa, nadzanena, Ine ndine Iye; nadzasocheresa ambiri, musawatsate pambuyo pawo. (Mat 24:4-5; Marko 13:5-6; Luka 21:8)

## 4 NKHONDO NDI MBIRI ZA NKHONDO

Ndipo m'mene mudzamva za nkhondo ndi mbiri zache za nkhondo, musadzadele nkhawa: Ziyenera kuchitika izi; koma sichinafike chimariziro. (Mat 24:6; Marko 13:7; Luka 21:9).

## 5 NKHONDO YAPACHIWENIWENI |ZIVOMELEZI | NJALA | MATENDA

Pakuti mtundu wa anthu udzayambana ndi mtundu wina, ndipo ufumu ndi ufumu unzache: padzakhala zivomelezi zazikuru, ndi njala ndi miliri m'malo akuti ndi akuti, ndipo kudzakhala zoopsya ndi zizindikilo zazikuru zakumwamba. (Mat 24:7; Marko 13:8; Luka 21:10-11)

## 6

Izi ndi zoyambira za zowawa. (Mat 24:8; Marko 13:8)

## 7 KUSAUTSIDWA KWA A KHRISTU

Koma inu mukhale atchelu, pakuti zisanachitike izi, anthu adzakuthirani manja, nadzakuzunzani, adzakuperekani inu ku ma sunagoge ndi ndende,adzakuperekani ku nsautso nadzakuphani, adzamukananu kwa mafumu ndi akazembe chifukwa cha dzina langa. Koma kudzakhala kwa inu ngati umboni (Mat 24:9, Marko 13:9, Luka 21: 12-13).

## 8

Ndipo pamene adzapita nanu ku mlandu, nadzakuperekani, musadzade nkhawa, tsimikizani mu mtima mwanu kuti usanafike mlandu musalingalile chimene mudzayankha. Koma chimene chidzapatsidwa kwa inu m'mphindi yomweyo, mudzayankhule, pakuti olankhula si inu, koma Mzimu Woyera. Pakuti Ine ndidzakupatsani inu kamwa ndi nzeru zimene adani anu onse sadzatha kuzikana kapena kuzitsutsa. (Marko 13:11, Luka 21:14-15)

## 9 KUTEMBENUKILANA MU MABANJA

Ndipo pomwepo ambiri adzakhumudwa, ndipo m'bale adzapereka m'bale wache kuti amuphe ndi atate mwana ache, abale ndi fuko lanu ndi abwenzi anu. Ana adzayambana ndi akuwabala nadzawaphetsa. Ndipo adzadana nanu anthu onse chifukwa cha dzina langa. Ndipo silidzaonongeka tsitsi limodzi la pamutu panu. Mudzakhala nawo moyo wanu muchipiliro. (Mat 24:9-10, Marko 13:12-13, Luka 21:16-19)

## 10 CHIKONDI CHIDZACHEPA

Ndipo chifukwa cha kuchuluka kwa kusa weluzika chikondano cha aunyinji chidzazirala. Koma iye wakulimbika chilimbikire kufikira kuchimariziro, yemweyo adzapulumuka. (Mat 24:12-13).

## 11

Ndipo **UTHENGA WA UFUMU WA MULUNGU** udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi ngati umboni kwa anthu a mitundu yonse, ndipo pomwepo chidzafika chimariziro. (Mat 24:14, Marko 13:10).

## 12 CHONYASA CHA KUPULULUTSA MU YERUSALEMU

Koma pamene mudzaone Yerusalemu atazingidwa ndi magulu a ankhondo, zindikirani pamenepo kuti chipululutso chache chayandikira (Luka 21:20). Chifukwa chache mukadzaona chonyasa cha kupululutsa chimene chidanenedwa ndi Danieli mneneri chitaima m'malo oyera ( iye amene awerenga m'kalata azindikire) pomwepo iwo ali m'Yudeya athawire kumapiri. Iwo ali mkati mwake aturuke ndi iwo ali kumiraga asalowemo. Iye amene adzakhala pamwamba pa nyumba yache asatsike kukatenga akutundu ache m'nyumba mwake. Iye amene ali m'munda chimodzimodzi asabwelere kukatenga chofunda chache (Mat 24: 15-18, Marko 13:14-16, Luka 17:31, 21:21). Koma tsoka ali nalo iwo akukhala ndi pakati ndi akuyamwisa ana m'masiku awo. Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusazakhale pa nyengo ya chisanu kapena pa Sabata ( Mat 24:19-20, Marko 13:17-18, Luka 21-23). Ndipo adzagwa ndi lupanga lakuthwa, nadzagwidwa ndende kunka ku mitundu yonse ya anthu, ndipo mapazi a anthu akunja adzapondereza kufikira kuti nthawi zawo za akunja zakwanira (Luka 21:24).

## 13 NTHAWI YA MSAUKO WA YAKOBO

(Yer 30:6-7)

Pakuti pomwepo padzakhala masauko akuru monga sipadakhalepo otelo kuyambila chiyambi cha dziko kufika tsopano. Inde ndipo sipadzakhalanso. Ndipo akadaleka kufupikitsidwa masiku awo, sakadapulumuka munthu aliyense; koma chifukwa cha osankhidwawo masiku awo adzafupikisidwa. (Mat 24:21-22, Marko 13:19-20, Luka 21:23). Chifukwa amenewa ndi masiku akubwezera, akuti zonse zidalembedwa zichitike (Luka 21:22).

## 14 AKHRISTU ONAMA NDI ANENERI ONAMA

Pomwepo munthu akanena kwa inu, onani, Khristu ali kuno, kapena uko musamuvomereze. Chifukwa Akhristu onama adzauka ndi aneneri onama nadzaonetsa zazikulu ndi zozizwitsa kuti akasocheretse, ngati nkutheka osankhidwa omwe. Koma yang'anirani, onani ndakuuzaniranitu zinthu zonse, zisanafike. (Mat 24:23-24, Marko 13:21-23) Chifukwa chache akanena kwa inu, Onani Iye ali m'chipululu; musapiteko. Onani ali m'zipinda; musavomereze. Pakuti monga mphezi idzera kum'mawa, nionekera kufikira kumadzulo; kotero kudzakhalanso kufika kwache kwa Mwana wa munthu( Mat 24:25-27, Luka 17:23-24)

## 15 ZIZINDIKIRO M'LENGALENGA

Koma pomwepo, akazatha masauko a masiku awo, dzuwa lidzadetsedwa, ndi mwezi sudzaonetsa kuwala kwache, nyenyezi zidzagwa kuchokela kumwamba, mphamvu za kumwamba zidzagwedezeka (Mat 24:29, Marko 13:24-25, Luka 21:25). Pa dziko la pansi, chisauko cha mitundu ya anthu, alikuthedwa nzeru, mkukumo wache wa nyanja ndi mafunde ache, anthu akumomoka ndi mantha ndi kuyembekezera zinthu zirinkudza ku dziko lapansi. (Luka 21:25-26).





16 Ndipo pompwepo padzaoneka m'thambo **CHIZINDIKIRO CHA MWANA WA MUNTHU**, ndipo mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzadziguguda pachifuwa, nadzapenya Mwana wa munthu alinkudza pa mitambo ya kumwamba, ndi mphamvu ndi ulemerero waukuru. Ndipo Iye adzatumiza angelo ache ndi kulira kwakukuru kwa lipenga ndipo iwo adzasonkhanisa osankhidwa ache ku mphepo zinai, kuyambira malekezero a dziko la pansi kufikira malekezero a thambo (Mat 24: 30-31, Marko 13: 26-27, Luka 21:27).

17 Koma poyamba kuchitika izi weramukani, tukulani mitu yanu; chifukwa chiomboledwe chanu chayandikira (Luka 21:28).

18 Ndipo ananena nao, phunzirani ndi mkuyu fanizo lache, pamene pafika kuti nthambi yache ikhala yanthete, ndipo aphuka masamba ache, muzindikira kuti layandikira dzinja, chomwecho inunso, **PAKUONA ZINTHU IZI ZIRIKUCHITIKA, ZINDIKIRANI KUTI UFUMU WA MULUNGU ULI PAFUPI,** uli pafupi ndi khomo (Mat 24:32-33, Marko 13:28-29, Luka 21:29-31). Koma za tsiku ilo, kapena nthawi yache sadziwa munthu, angakhale angelo m'Mwamba, koma Atate okha (Mat 24:36, Marko 13-32).

19 Ndipo monga **MASIKU A NOWA,** kotero kudzakhala kufika kwache kwa Mwana wa munthu. Pakuti monga m'masiku aja, chisanafike chigumula, anthu analinkudya ndi kumwa, anali kukwatira ndi kukwatiwa kufikira tsiku limene Nowa analowa m'chingalawa. Ndipo iwo sanadziwe kanthu, kufikira kumene chigumula chinadza, chinapululutsa iwo onse, kotero kudzakhala kufika kwache kwa Mwana wa munthu (Mat 24:37-39, Luka 17: 26-27).


Onerani Angel Tv
www.angeltv.org

Satellite : INTELSAT 20 (IS20)
Orbital Location : 68.5° East
Band : Ku-Band
Downlink Frequency : 12.522 GHz
Polarization : Vertical
Symbol Rate : 27.500 Msps
FEC : 3/4
Modulation : DVB-S, MPEG-2 / SD
Coverage Area : AFRICA & EUROPE


20 Monga momwemoso kunalili **MASIKU A LOTI,** anadya, anamwa, anagula, anagulitsa, anabzala, anamanga nyumba, koma tsiku limene Loti anatuluka m'Sodoma udavumba moto ndi sulfure zochokera kumwamba, ndipo zinawaononga onsewo, momwemo kudzakhala tsiku lakuvumbuluka Mwana wa munthu (Luka 17: 28-30).

21 Kumbukilani mkazi wa Loti. Iye aliyense akufuna kusunga moyo wache adzautaya, koma iye ali yense atadzautaye, adzausunga (Luka 17: 32-33).

22 Ndinena ndi inu, usiku womwewo adzakhala awiri pa kama limodzi, m'modzi azatengedwa, ndi wina adzasiyidwa. Padzakhala akazi awiri akupera pamodzi, m'modzi adzatengedwa. Pomwepo adzakhala awiri m'munda, m'modzi adzatengedwa, ndi wina adzasiyidwa (Mat 24: 40-41, Luka 17: 34-36). Ndipo anayankha nanena kwa Iye," kuti, Ambuye?" Ndipo anati kwa iwo pamene pali mtembo, pomweponso miimba idzasonkhanidwa (Mat 24:28, Luka 17:37).

23 **KHALANI ATCHERU NDI AKUPEMPHELA**
Monga ngati munthu wa paulendo, adachoka kunyuma kwache, nawapatsa akapolo ache ulamulilo, kwa munthu ali yense ntchito yache, nalamulila wapakhomo adikire. Chifukwa chache dikirani; pakuti simudziwa inu nthawi yache yakubwera mwini nyumba, kapena ndi madzulo, kapena ndi pakati pausiku, kapena pakulira tambala, kapena mmawa; kuti angabwere balamanthu nakakupezani muli m'tulo (Marko 13: 34-36).

24 Koma dziwani ichi, kuti mwini nyumba akadadziwa nthawi yiti mbala ikudza, iye akadadikira, ndipo sakadalola kuti nyumba yache ibooledwe. Chifukwa chache khalani inunso okonzekeratu; chifukwa munthawi imene simuganizira, Mwana wa munthu adzadza (Mat 24: 43-44).

Local Contact Address

25 Koma mudziyang'anire nokha, kuti kapena mitima yanu ingalemetsedwe ndi madyaidya ndi kuledzera, ndi zosamalira za moyo uno, ndi kuti tsiku ilo lingafikire inu modzidzimutsa. Yang'anirani, dikirani, pempherani: pakuti simudziwa nthawi yache. Pakuti lidzakhala ngati msampha, lidzatero ndi kufikira anthu onse akukhala pa nkhope pa dziko lonse lapansi (Marko 13:33, Luka 21: 34-35).

26 Koma inu dikirani nyengo zonse, ndi kupemphera, kuti mukalimbike kupulumuka zonse zimene zidzachitike, ndi kuimirira pamaso pa Mwana wa munthu (Luka 21:36).

27 Indetu ndinena kwa inu, mbadwo uwu sudzatha kuchoka kufikira zinthu zonsezi zidzachitidwa (Mat 24:34-35, Marko 13:30-31, Luka 21: 32-33).


**Yakhala pa mpando Wache wachifumu waulemerero, Mfumu Yaikuluyo**-Ambuye Yesu Khristu akubwelaso posachedwapa ndi mphamvu zazikulu ndi ulemerero pamodzi ndi angelo ache oyera ndi anthu oyera.

**Opani Mulungu, mpatseni ulemerero; pakuti yafika nthawi ya chiweruziro chache, ndipo mlambireni Iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi akasupe amadzi ( cibv 14:7).**

## SIPADZAKHALANSO NTHAWI!

**Ufumu wakumwamba wayandikira tsopano. Lapani ndi kukhulupirira uwu uthenga Wabwino.**

**Konzekani kukakuma ndi Ambuye Mulungu wanu!**



# UTHENGA WABWINO WA UFUMU WA MULUNGU

**CHICHEWA | AFRICA**